

Danieli : 7:1-6

Mutu : Masomphenya a Danieli a zirombo zinayi

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero titsogozedwe ndi mau a Mulungu amene ali pa 1 Akorinto 4:5, amene akuti, “Chifukwa chake musaweruze kanthu isanadze nthawi yake, kufikira akadze Ambuye, amenensoadzaonetserazobisika za m’dima, nadzasonyezazitsimikizo za mtima.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 7:1-4, m’mene timakambirana za masomphenya a Danieli a zirombo zolusa. Ndipo lero pa Danieli 7:1-6, tipitiliza kuona masomphenya a Danieli a zirombo zinayi.

Danieli 7

Masomphenya a Danieli a zirombo zinayi

Mfumu Nebukadnezero ya Babulo inali ya nzeru kopambana, amene anadzitengera yekha ufumu ndi kudzikweza pokhala mfumu yoyamba yaikulu ya dziko lonse lapansi. Ndikunena mau amenewa

chifukwa chakuti ndiye amene anakwanitsakukuza ufumu wake m'maiko atatu akuru-akuru monga a Asia, Europe ndi Aigupto ku Africa. Kutsimikiza kuti Nebukadnezara anali ndi ufumu waukulu padziko lonse lapansi. Koma Nebukadnezara sanali kudziwa zomwe zidzachitika m'tsogolo ku ufumu wakewo. Apa, ndipo pamene analota loto la fano lopangidwa ndi miyalayosiyana-siyana, lomwe Danieli anatanthauzira (Danieli 2).

Mukumbukira kuti mu loto lake, munali zitsulo za mitundu inayi osati isanu ayi. Ndipo masomphenya a Danieli munalinso zirombo zinai; zomwe ndi mkango, chimbalangondo, kambuku ndi chirombo china chomwe chinali ndi maonekedwe oopsa chokhala ndi nyanga khumi. Ichi chinali chirombo chomwe chinali choopsa m'maonekedwe ake, chimene sichinakhalepo padziko, m'madzi ndi mlengalenga momwe.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti pamene Danieli anali m'dzenje la mikango adagonatulo, koma pano pamene waona masomphenya awa, wasoweratutulo. Taonaninso kuti Danieli anasauka mumtima mwake pamene Mulungu adapereka loto ndi kumasulira kwake lomwe mfumu Nebukadnezara analota. Ichi,

ndichifukwa chakuti Danieli ngati mu Yuda amene amadziwa lonjezo lomwe Mulungu adachita ndi Davide, kuti kudzera ku muzu wake, mfumu ya dziko lonse idzabadwa. Ndiye pa loto la Nebukadnezzara lofotokonza maufumu anayi a dziko lonse lapansi, anasauka kudziwa momwe Mulungu adzakwaniritsira lonjezo lake la mfumu amene adzabadwakwa Davide. Tere kuyambira pano kufika kumapeto a bukuli, tiona yankho lafunso la Danieli.

1. Chaka choyamba cha Belisazara mfumu ya ku Babulo Danieli anaona loto, naona masomphenya a m'mtima mwake pakama pake; ndipo analemba lotolo, nalifotokonzero, mwachidule.

Pano ndifuna ndiyambe ndi mau akuti nthawi yomwe masomphenya awa anaoneka, ikudziwika bwino kuti inali m'chaka choyamba cha mfumu Belisazara. Uku, ndiko kumapeto kwa ulamuliro wa Babulo, yemwe ndi mutu wa golidi, amene analamulira dziko lonse lapansi. Koma taonani kuti Gobrusi, mkuluwa nkhondo wa Amedi, anadza ndi kulowa panso pa mzinda wa Babulo kudzera mu mtsinje wa Euphrates, pamene mfumu Belisazara anali kulamulira mu ufumu wa Babulo.

Nkhani ili mundime ino ikuti, tsiku lina lake Danieli ali chigonilepakama pake Mulungu analankhula naye kudzera m'amasomphenya.

Tsono pamene Danieli anaonetsedwamasomphenyawa, anawalemba ndi cholinga chakuti agwiritse ntchito patsogolo pake ndikutiasaiwale. Komanso anapereka lotolikwa abale ake, a Yuda ndi cholinga chakuti aphunzitse ana awo komanso kuti akhoze kuphunzitsa chimenechi kwa iwo ali kutari. Tsono Danieli anapereka loto limeneli kwa a Yuda anzake chifukwa panapezeka kuti a Yudawosanamvetsetse ulosi wa Yereimiya ndi Ezeikieli chifukwa anamasulira kuti pamene iwo adzabwerera kwawo, kwawoko adzakhala paufulu ndi mtendere weni-weni. Tere, uwu ndiwo Uthenga umene Danieli akupereka kuti sayenera kudziyenga wokha chifukwa mwa masomphenya awa, Mulungu akuwaonetsera kuti adzakumana ndi masautso ndi kuzunzika kwakukuru. Ndipo ichi, chiyenera kuti chichitikemwakuphunzitsa komanso kuwerenga mau a masomphenyawo.

2. Danieli ananena, nati ndinaona m’masomphenya anga usiku, taonani mphepo zinayi za mu mlengalengazinabuka pa Nyanja yaikuru.

Poyamba ndifuna tigwire mau akuti, “Mphepo zinayi za mu mlengalengazinabuka pa Nyanja yaikuru.” Kunena kuti mphepo inali kuomba pa nyanjayaikuru ya Mediterranean. Tsono mphepo imaimira mtima woukira, wamikanganowosokeretsa ndi kusokoneza maganizo ya anthu. Ndipo pamene tikamba za “Nyanja” tikuona kuchuluka kwa anthu, zigawenga ndi anthu amitundu ina (Mateyu 13:47; Chibvumbulutso 13:1, Yesaya 57:20). Awa, ndiwo anthu amene akutchulidwa pa Chibvumbulutso 17:1, 15, pamene pali mau akuti, “Ndipo anadza m’modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsachitsutso cha mkazi wa chigololo wamkuru, wakukhala pa madzi ambiri. Ndipo anena ndi ine, madziwoudawaonaukoakhalako mkazi wachigololo ndiwo anthu ndi makamu ndi mitundu ndi manenedwe.”Kutsindika kuti madzi ambiri kapena Nyanja ikuimira anthu ambiri mitundu ya anthu ndi zilankhulochosiyana-siyana.

Ndiye tikaonetsetsa mphepo imakondakuomba kuchokera ku dera limodzi ndi kupita kudera limodzinso. Koma pano pakuonetsa kuti pali mphepo yamkuntho yomwe yomwe ikuchokera mbali zonse ndi ndiyoononga zinthu. Tsono tiyenera kudziwa kuti mphepo iyi, sikungosonyeza maufumu anayi wokha komwe kukuchokera chisautso chimenechi ayi, komanso kugawo lotsiriza la ufumu wachinayi (vv. 11, 12, 17), lomwe muli ziphunzitso zina zomwe zidzakopa ndi kusokoneza maganizo ya anthu amitundu ina ndi mapfuko ake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano ndikunenetse kuti inu ndi ine, tiri m'gawo lotsiriza la ufumu wachinayi. Kunena kuti nthawi ikuyandikirakunyengo yomwe ufumu wa Aroma udzamangidwanso, kotero kuti pakungofunika munthu amene adzakhazikitse ufumu umenewu. Tikunena kuti mitundu yonse ya anthu idzasonkhanitsidwa pamodzi ndi ziphunzitso zawo, kayendetsedweka Bomakawo ndi malingariro awo. Kutanthauza kuti maiko onse pansi pano atseguka m'maso, kotero kuti munthu aliyense akufunitsitsakuchitanawo chinthu chilichonse chatsopano. Kunena kuti anthu akhala osadziwa zinthu zambiri,

koma pano aliyense wasinthika kapena kuti wachangamuka chifukwa cha mawailesiakanema ndi omvera, mafoniapamwamba ngakhaleenso zida za nkhondo ndizapamwambazedi. Nkhani yonseyi ikunena kuti maganizo a tsopanowam'mawailesi ndi Television ndiwo amene akopa anthu ochuluka ndipo dzikoli ladzala ndi maganizo achinyengookha-okha, amene achotsa chiphunzitso cha mau a Mulungu. Tsono iyi, ndiyo nthawi yabwino yomwe atumiki a Mulungu ayenera kukangalika kupereka Uthenga Wabwino wa choonadi cha Mulungu.

Ndiye pamene tiwerenga verse 8, tipeza mau akuti, "Ndinalikulingirira za nyangazi, taonani, pakati pa izo panaphukanyanga yina, ndiyo yaing'ono; patsogolo pake zitatu za nyangazoyambazizinazulidwa ndi mizu yomwe; ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa palikunena zazikuru." Mau amenewa akutanthauza kuti nyangayaying'onoyindiyomweidzakwaniritsakunyenga kapena kupotoza maganizo ya anthu ambiri. Uyu, ndiye munthu wotchedwa satana, amene adzadzionetsera yekha kudziko pamene akubwera. Ichi, ndichimene Ambuye wathu Yesu Kristu, anali

kunena pa Yohane 5:43, pamene anati, “Ndadza Ine m’dzina la Atate wanga, ndipo simundilandira Ine; akadza wina m’dzina lake la iye mwini, iyeyu mudzamlandira.”

Lero anthu akulemekeza munthu koposa Mulungu chifukwa chinthu chosangalatsa munthu lero ndi munthu mnzake. Taonani momwe anthu amachitira chidwi ndi anthu amene achita masewera osiyana-siyana. Mwachitsanzo anthu amaika chidwi pa osewerampira komanso ochitazisudzo. Koma aiwala kuti ndi masewera kapena zisudzozomwezi zimene zinaononga makhalidwe ya a Greek. Ndiye tikunena kuti kukanakhala bwino munthu akanaonongeka kapena kuti maganizo a munthu akanadzazidwa ndi mau a Mulungu. Kutsimikiza kuti mphepo ya mkunthoyayamba kale kuomba pa Nyanja (anthu ambiri). Kunena kuti zinthu zayamba kale kusintha ndipo zikupitakoipa.

3. Ndipo zinaturukam’nyanja zirombo zazikuru zinayi zosiyana-siyana.

Pano pali chithunzi cha nyama zinayi zosiyana-siyana zomwe zikuimira maufumu osiyana-siyana, amene anabuka kapena kukhazikitsidwa padziko m’nthawi yosiyana-siyana. Ndiye cholinga

choonetsa ufumuwu ndi chofuna kuonetsa kuti ufumuwu unali kukhazikitsidwa pamene panali kusagwirizana ndi chisokonezo pakati pa mitundu ya anthu. M'chitidwe uwu, ndiwo umene ukuonetsedwa mwakudzaza ndi kuwindukakwa Nyanja. Uwu, ndiwo ufumu wa Babulo, Peresiya, Greako ndi Roma, umene ukuonetsedwa ndi mphamvu komanso ukali wa nyama zosiyana-siyana.

4. Choyambachinangamkango chinali nawo mapiko a chiombankhanga, ndinapenyera mpaka nthenga zake zinathothoka, nichinakwezekakudziko ndi kuimitsidwa ndi mapazi awiri ngati munthu nichipatsidwa mtima wa munthu.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti maufumu anali kuimiridwa ndi mitundu yosiyana-siyana ya nyama popeza ukali ndi kuopsakwanyamazi kunali kuonetsa mtundu wa ufumu umene unakhazikitsidwa panthawi imeneyo. Nyama izi, zinali kusiyana m'maonekedwe, mphamvu ndi mtundu wake kuonetsa mtundu wa ufumu ndi mtundu wa anthu amene akulamulirawo.

Tsono nyama yoyamba ndiyo imene inali kuoneka monga mkango. Mkango uwu, ndiwo wachilendo chifukwa uli ndi mapiko a

chiombankhanga. Maonekedwe awa, ndiwo akungoonetsa mphamvu ndi kukhazikitsidwa mofulumira kwa ufumu wa Akasidi (Babulo). Tsono kukhala ndi asirikari a mphamvu ndi kutenga ulamuliro wamadera ena, mofulumira ndicho chinsinsi cha ufumu wamphamvu m'mbiri ya dziko. Tamvani mkulu wina wa Asirikari, wotchedwa Nathan Bedford Forrest, atafunsidwa za chinsinsi chakuti azipambana nkhondo, adanena kuti, "Munthu amene angafikepamalopo mofulumira natengazochuruka, ndiye amapambana nkhondo." Tere ichi, ndicho chinali chinsinsi cha asirikari a mfumu Nebukadnezara, amene anali ndi lunthalofika pamalo mofulumira ndi kutenga ulamuliro wamalowo. Tere mfumu Nebukadnezara anakhala mfumu yamphamvu padziko lonse lapansi chifukwa cha chinsinsi chimenechi. Momwemonso ichi, chinali chinthu chimene chinathandizira kuti Alexander the Great, a Kaisara onse a Roma ndi Napeleon Bonapatte akhazikitse ufumu wamphamvu mofulumira. Ndiye tiyenera kudziwa kuti Ufumu wa uwu, unali kupereka mphamvu zochuruka ku mafumu awo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, mkango ndicho chizindikiro cha ufumu kapena mfumu amene amadziwika bwino ndi mphamvu,

kugonjetsa maufumu ena, monga muja uchitiramkangokugonjetsa nyama zizake.

Ndiye taonani kuti mapiko amene anali ndi mkango uwu, ndiwo amene akuonetsa kuti Babulo anali kuuluka kapena kuthamanga kulanda ndi kutenga ulamuliro pa ufumu wina. Koma taonani Danieli akuona kuti mapiko aja akuchotsedwapang'onopang'ono. Uku, kunali kuthakwa ulamuliro wa Babulo popeza Mulungu anamuchotsera nzeru Nebukadneza. Kutanthauza kuti maufumu amene anali pansu paulamuliro wake, anachoka ndi kukhala ndi ulamuliro pa iwo wokha.

Mau akuti, "...ndi kuimitsidwa ndi mapazi awiri ngati munthu, nichinapatsidwa mtima wa munthu." Awa, ndiwo mau amene akuonetsa kubwezeretsedwakwa mfumu Nebukadneza ku munthu wake, amene anali ngati nyama yakuthengo. Kutanthauza kuti tsopano Nebukadneza sakhoza kuchita mwamphamvu ndi moopsa monga muja anali kuchitira m'mbuyomo ayi. Tere pano ndi munthu amene ali ndi mphamvu komanso nzeru yofooka ya munthu wamba. Apa, ndipo pamene

ndikukhulupirira kuti Nebukadnezara anafika pokhulupirira Mulungu m'modzi wamoyo.

Ndiye tikunenetsa kuti mkango ndiwo umene ukuimira mutu wagolidi, mutu wamphamvu, umene lero lino ndilo bwinja monga momwe mneneri Yeremiya analosera. Ichi, ndicho chitsimikizo chakuti ulemerero wathupi kapena ulemerero wakunja umakhala wanthawiyochepa. Tere, pamene mkangoukuimirapabwinja la ufumu wamphamvuwu, zikuonetsadi kuti ufumu wa Babulo unali wolimba komanso wamphamvu.

Ndiye tikunetsakuti, ufumu wa Babulo unathyoka chifukwa chakuti Mulungu Wamkulu-kulu adana ndi mtima wodzikweza. Taonani Nebukadnezara anatsitsidwa ndi kufika pobvomereza kuti ndi Mulungu wachita izi. Tamvani mau amene Nebukadnezara adanena pa Danieli 4:35, pamene anati, “Ndi okhala pa dziko lapansi onse ayesedwaachabe; ndipo Iye achita mwa chifuniro chake m'khamu la Kumwamba ndi mwa okhala pa dziko lapansi; ndipo palibe woletsa dzanja lake, kapena wakunena naye muchitanji?”

Ndiye tikunenetsa kuti pamene mutu wa golidi ukuonetsa ulemerero wakunjawachitukuko cha dzikoli, momwemonso kuopsa kwa maonekedwe a mkangokukufotokonzerakukula ndi kuopsa kwa moyo wachikunja komwe kunali muufumu umenewu. Uku, ndiko kuopsakwa moyo wodzikweza.

5. Ndipo taonani, chirombo china chachiwiri chikungachimbalangondochinatundumukambali imodzi; ndi m'kamwa mwake munali nthiti zitatu pakati pa mano ake; ndipo anatero nacho, nyamuka, lusira nyama zambiri.

Tsono chimbalangondo ndiyo nyama yomwe ikuimira ufumu wa Amedi ndi Peresiya, umene unafanizidwa ndi manja a siliva mu fano la Nebukadnezzara. Ndiye pamene tikunena kuti chimbalangondochinatundumukambali imodzi, tikunena kuti dzanja limodzi lomwe ndi ufumu wa Amedi, linakantha ndi kugonjetsa Babulo. Izi, zinatsagana ndi kumenyedwakwa Aigupto ndi a Peresiya zomwe zinapangitsa kugwa kwa ufumu wonse wa Babulo. Ndiye Uthenga ukunena kuti kukanthidwamwaukari ndi kutengedwa kwa ulamuliro kukufananandi kukanthidwa ndi chirombocholusa monga momwe achitira anthu woipa.

6. Pambuyo pake Ndinapenya ndi kuona china ngati nyalugwe, chinali nawo mapaiko anayi ankhukupamsana pake, chirombocho chinali nayonso mitu inayi, nichinapatsidwa ulamuliro.

Chirombo chachitatu ndicho nyalugwe, chomwe chikuimira ufumu waGreako, umene unakhazikitsidwa ndi Alexander the Great. Uyu, ndiye munthu amene anali wachangu, wochenjera ndi wankhanza monga nyalugwe. Taonani nyalugwe uyu, anali ndi mapiko anayi, pamene mkango unali ndi mapiko awiri, kutanthauza kuti Alexander ndiye amene anamenya nkhondo ndi mphamvu kuposa Nebukadnezzara. Tere mitu inayi ikuonetsa kugawikakwa ufumu wa Alexander panthawi ya imfa yake.

Tsono ndifuna muone kuti ufumu wa Babulo unagwa chifukwa cha vinyo momwemonso ufumu wa Alexander. Ndiye inu mukaona dziko lathuli likupita kuti ndi m'chitidwe wauchidakwawu?

7. Pambuyo pake ndinaona m'amasomphenya a usiku, ndi kuona chirombochachinayi, choopsa ndi chochititsa mantha ndi champhamvuchoposa, chinali nawo mano akuru a chitsulo, chinalusa ndi kuphwanya ndi kuponderezachotsala ndi

mapazi ake; chinasiyana ndi zirombo zonse zidachitsogolera;
ndipo chinali ndi nyanga khumi.

Tsono chirombo chomwe sichikudziwikachichikuimira ufumu wa Roma, umene unaonetsedwanso ndi miyendoyachitsulo mu fano la Nebukadnezzara. Ichi, ndichirombo chachilendo popeza nyama zina monga mkango, chimbalangondo ndi nyalugwe, ziri ndi zizawokutchire, koma simungathe kupeza nyama yofanana ndi chiromboichi kutchire. Kutsimikiza kuti ndiyo nyama yachilendoyokhala ndi nyanga khumi, imene ikufanana ndi fano la zala khumi. Ndiye tikunena kuti masomphenya awa, sakufotokonza za chiyambi cha ufumuwu ayi, koma akuonetsa nthawi ya masiku otsiriza. Kutanthauza nthawi ya masiku a nyanga khumi ndiyo yofunika kwambiri chifukwa ndiwo masiku amene asanakwaniritsidwe.

Wokondedwa anzanga apaulendo tiyeni titsirize ndi mau akuti, masomphenya a nyanga zitatu, anakwaniritsidwa kale kotero kuti chatsala ndi kukwaniritsidwa kwa nthawi ya nyanga khumi. Tikunena kuti ufumu wachinayiwa Roma unakhazikitsidwa kale, ngakhale kuti unagwa kale. Uwu, udzaukanso pamene

udzaonekera mwa maufumu khumi.Ufumu uwu,
udzasonkhanitsidwanso pamodzi ndi yemwe mau a Mulungu
akumutchulawotsutsa Kristu.

Kwalerotilekeza pano ndipo tinali kusanthula Danieli 7:1-6,
timapitiliza kuona masomphenya a Danieli a zirombo zinayi.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!